Alipo magulu amene angathe kukuthandizani mutagwe mmavuto. Makeyala ao ndi awa:

Ku Holland:

Foundation of the Religious Against Trafficking in Women

Sint Janssingel 92
NL 5211 DA Den Bosch
Nederland
Tel: (+31) 73 – 615 44 44
Fax: (+31) 73 – 615 44 49
E-mail: srtv@srtv.info
Website: www.srtv.info
Bankgiro: 420557 t.n.v. SRTV
KvK 34156001

Solwodi (Solidarity with Women in Distress)
Probstei-Strasse 2
D-54154 Boppard Hirzenach,
Germany
Tel.+49-67 41 22 32
Fax: +49-67412310
E-mail: solwodi@t-oneline.de
www.solwodi.de

MOTI KU ULAYA NKUPALADIZO ?

MUSAKHULUPILIRE NKHANI ZABODZA !

CHICHEWA (MALAWI)

Kodi wina wake adakulonjezani zoti mudzasanduka

OLEMERA NDI APAMWAMBA MUKAPITA KU ULAYA?

CHENJEZO KWA AMAYI ONSE !

NKHANIYI NDI YA ASUNGWANA NDI AZIMAYI A KU MALAWI POWAFOTOKOZERA ZOOPSA ZINA ZOMWE ANGAKOMANE NAZO KU ULAYA.

MVERANI NKHANI

Za azimayi anzanu amene adaganiza kupeza ntchito yabwino ku ulaya …..

NANGONDO
Iye analephera kupeza ntchito kwao ku Malawi kuti athandize mwana wake ndi makolo osauka. Tsono njonda ina inamunamiza kuti imulemba ntchito yovina gule wamakolo ku Holland. Koma zonsezi sizinachitike, mmwalo mwake anamuirizidwa kungolowa mbala nkumachita uhule.

NTCHAWAKA
Uyu amalemberana makalata ndi mkosana wina pokhulupirira kuti ndi wolemera ndipo atha kukwatiwa naye. Bwenzi lakelo linamuitana kuti apite ku Germany. Atafikako anadabwa poona kuti mwamunayo anali nkhalamba yotheratu ndiponso chidakwa. Tsiku lirilonse Ntchawaka amangomenyedwa.

LITA
Dolo lina la ku Belgium linamunyenga Lita kuti lidzamulemba ntchito ya ulembi mu Hotela yake. Koma Lita atafika, analandidwa chitupa chake choyendera nkumuumiriza kuti azichita uhule.

Pepani, nkhani za ukapolo wotere zilipo zambiri.

Wopatsa pepala lino ali wokonzeka kufotokoza koposa ndi kukuthandizani.

CHIFUKWA CHOPERKERA CHENJEZOLI NCHITI ?

Ku Ulaya timakumana ndi asungwana ndi amayi osauka ndi ovutika, ochokera ku Africa ndi kwina, kumene analonjedwa kuti

* adzapeza ntchito yapamwamba,
* adzalandira malipiro okwera,
* adzapeza banja labwino,
* ndi zina zotere.

Tsono amakhulupirira kuti atha kupezachuma pa kanthawi kochepa kuti choncho akabwerera kwao athandize abale ao osauka.

KOMA ZOONA ZENIZENI NZITI ?

1. Ku Ulaya alipo anthu ambiri osowa ntchito. Nanji Inu, mlendo, wosadziwa chilankhulo ndi mwambo wa komweko, mudzavutika koposa kuti mudzapeza ntchito yabwino.

2. Kumafunika chilolezi choloweramo mdziko (entry permit) ndi zilolezi zina zambiri zogwira ntchito (work permit).

3. Amayi ambiri monga inu, akapeza ntchito, malipiro ao ndi ochepa kwambiri. Tsono chifukwa cha kuvitika kotere amangothamangira kukagulitsa matupi ao.

4. Anthu onyenga amalonjeza zambiri ndiponso zokoka makutu anzao. Koma zonsezi nzabodza. Chenjerani !

Musamapite ulendo ngati simunalandira poyamba zilolezi zonse zofunika !

NGATI MUKUFUNABE KUPITA ONETSETSANI KUTI:

1. Mukudziwa maina ndi keyala ya anthu omwe akukuitanani.

2. Mufufuze ku Ambasi (Embassy) ya dziko lomwe mukunkako ngati okulembani ntchito ali anthu okulupirika ndi okhala ndi zilolezi zovomerezeka.

3. Mudziwane ndi magulu a dziko lanu, oyang' anira anthu olowa ndi otuluka dziko, kuti pobwerera musadzavutike.

4. Mudziwitse abale anu za tsiku lonyamuka keyala ya komwe mukupita, chithunzi chanu cha pasipoti ndiponso maina a anthu amene muli nao pa ulendowu.

PASIPOTI YANU NDI YANU !

5. Mukagwe mavuto, ngakhale mutakhala kuti mwalandidwa kale pasípoti (chitupa chanu choyendera), musaope kupempha chithandizo cha wokuimirirani pa mlandu, akuti lawyer.

6. Potsata Malamulo ovomerezedwa mdziko lonse la pansipano, munthu aliyense angathe kuumirira kuti alandire chithandizo chotere pakati pa mavuto ake.

Musayerekeze kupereka pasipoti yanu kwa wina aliyense !